

Maphunziro
a
Alangizi othandizira
alimi a ziweto m'midzi

Zida zogwiritsira ntchito
pa umoyo wa ziweto

Small Scale Livestock and Livelihoods Program
PO Box 1604, Lilongwe Malawi



Zida zogwiritsira ntchito pa umoyo wa ziweto

Phunziro 1: Zida zofunika pa umoyo wa ziweto

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. Kudziwa zida zofunikira pa za umoyo wa ng'ombe
2. Kudziwa kugwiritsa ntchito zida zothandizira pa za umoyowa ziweto

Zida zogwiritsa ntchito a vetenare

- Pali zida zambiri zimene ogwira ntchito ya vetenare ayenera kukhala nazo kuti agwire bwino ntchito yake.
- Chida choyesera kutentha kwa m'thupi ndi moikamo mwake. (*Thermometer with carrying case*)
 - Chida cha *thermometer* ndi chofunika kwambiri ndiye chiyenera kusamalidwa mwaukhondo ndi kuikidwa pamalo poti chisaphwanyike.
 - Musamasiye *thermometer* pamalo otentha pa dzuwa chifukwa itha kutentha ndi kuonongeka.
- Nyereti ndi zingano.
 - Zida izi ziyenera kugwiritsidwa ntchito ndi alangizi a za ziweto ndi ena ophunzitsidwa bwino.
 - Mothira mankhwala a nyereti amapangira pulasitiki kumene amaikako zingano. Pali mitundu iwiri ya kumilomo yoikako zingano za nyereti ndipo muonetsetse kuti zingano yagwira bwino kumlomo wa nyereti musanagwiritse ntchito.
 - Kukula ndi kotalika kwa zingano za nyereti ndi kofunika pakabayidwe kosiyanasiyana ka nyereti. Ma zingano wochepa mphipi ndipo ndi atali, amagwiritsidwa ntchito pobaya nyereti ya mu m'nofu. Pamene mazingano afupi amagwiritsidwa ntchito pabaya nyereti ya m'khungu. Mukafuna kukhala ndi manyereti ndi ma zingano oyenera, mufunse upangiri kwa dokotala wa vetenare.




- Botolo lomwetsera mankhwala

- Mutha kugwiritsa botolo lililonse lalitali khosi pomwetsa chiweto mankhwala. Mutha kulumikza kukamwa kwa botolo ka paipi (kachubu) kotalika ma sentimita 20 kuti mumwetse bwino mankhwala chiweto.



- Zida zothenera a tonde/nkhuzi

- pali timpeni totchedwa scalpel blade, lumu, mbano, ndi mphira.



- Chida chochosera nyanga (mphondo)

- Chipangizo ichi chimagwiritsidwa ntchito pamene mphondo zikuyamba kutuluka kumene. Chipangizo chimenechi chigwiritsidwe ntchito ndi munthu wophunzitsidwa bwino.

- Chipangizo chopanira mphuno za ng'ombe pofuna kuti isamapalapate pamene ikulandira chithandizo cha mankhwala.

- Chipangizo chogwailira nkhumba pamene ikulandira chithandizo cha mankhwala.

- Mipeni yakuthwa, ndi ma *scalpel blades*

- Zida izi ndi zifunika potumbula zilonda ndi zithupsya, kuthenera a tonde ndi ntchito zina zofunika kumbula. Mutha kugwiritsa ntchito lumu lakuthwa ndi la ukhondo.

- *Trocar* ndi *canula*

- Zida izi amene amagwiritsa ntchito ndi mlangizi wa za ziweto kapena munthu wina ali yense amene waphunzitsidwa bwino.

- Chida ichi ntchito yake ndi yochotsera mphepo mchife pamene chiweto chatupidwa kapena kudzimbidwa.

- Zingwe zomangira chiweto

- Zingwe ndizofunika pomangira ng'ombe pofuna kuziteteza ndi kudziteteza poziyendetsa, pozibaya pozipatsa mankhwala, pozithena ndi ntchitozina zotere.

- Zowengera ziboda ndi zodulira zikhadabo ndi mano

- Zida ndi zofumika powenga ziboda zomwe zakula ndi kutalika kwambiri kwambiri. Zikhadabo ndi mano a ziweto zina zimafunika kudula. Ndiye zida zodulira zilipo.

- Mabotolo oikamo mankhwala otsukira zida a *tincture of iodine* ndi *alcohol* otsukira zida.
 - Zida izi ndi thonje, ma bandenji, mwere ndi nsaru za ukhondo za thonje ndi zofunika pa zilonda.
- Pafunikanso kukhala ndi chikwama cholimba cha chikopa kapena kanavasi chotengera ndi kuikamo zida zimenezi kuti zitetezedwe ndikuti zizikhala zouma nthawi zonse.
- Pafunikanso kukhala ndi zobvala zogwilira ntchito monga jombo ndi *dust coat*.